

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

MALANGIZO NDI CHILIMBIKITSO KUCHOKERA M'BAIBULO
KUPITA KWA AMENE AKULALIKIRA UTHENGA WABWINO


“PITA IWE, NUCHITE MOMWEMO.”

(Nkhani yotsatirayi ikulongosola tsatanetsatane wa fanizo limene Yesu adanena pa Luka 10:25-37).

Munthu wa Chiyuda uyu anali thapsaa pansi, ali pafupi kufa, panjira yafumbi yochoka ku Yerusalemku kuita ku Yeriko. Iye anali atamenyedwa ndipo amangochucha magazi. Analu anamulanda katundu wake yense ndipo anali anamuvula zovala zake zonse, ntchentche zinali ng'waaaaa ndipo zimayamwa zilonda zake pamene dzuwa limaomba pa thupi lake. Popeza sakana kudzithandiza yekha, thupi lake linanka lifookera-fookera.

Kenaka kuwala kwa chiyembekezo kunawunikira mu ululu wake komanso kukomoka kwake pamene anazindikira kuti pali munthu wina amene akuyandikira. Thandizo likubwera tsopano. Wansembe, wodziwika bwino lomwe kuti ndi mtumiki wa Mulungu, anadutsa pamenepo; koma atamuona munthu wofuna chithandizo uja, analambalala ndipo sanafune kuti ulendo wake usokonezedwe ndi ntchito yosakondweretsayi. Choncho iye anapitirira ulendo wake, osalabadira za munthu wofuna kufa uja. Patangopita kanthawi, Mlevi amene amatumikira ku Nyumba ya Mulungu anadutsa. Nayenso anaima ndi

kumuona munthu wopwetekedwa uja, mmene amabuulira, ali mabala okhaokha. Anangotsonya nkuwloloka msewu kenaka napitirira ulendo wake.



Tsopano moyo umachoka mthupi lake pamene mabala aka anapitirira kuchucha magazi. Iye anamva ludzu, anali wotopa ndipo tsopano anali wopanda chiyembekezo pamene “anthu achipembedzo” amangomudutsa osamuthandiza. Iye anaulandira mdima wa imfa umene unamukuta ngati njira

yokhayo imene ingamuthandize kuti apulumuke ku kuzunzika kwake.

Mwadzidzidzi munthuyo anamva wina wake akumukhudza ndi kumanga mabala ake. Mutu wake unadzutsidwa ndipo anamva chapatali mau akunena kuti “Imwa mnzanga ‘we.’” Madzi ozizza bwino anayenda natsikira ku m’mero kwake. Moyo unayamba kubwerera m’tupi lake ndipo anazindikira kuti Msamariya ndi amene amamuthandiza. Asamariya anali anthu onyozedwa ndi osalidwa ndi Ayuda, koma Msamariya uyu ndi amene amapulumutsa moyo wake.

Msamariya uja anakweza munthu waChiyuda uja pa bulu wake namutengera ku nyumba ya Alendo. Tsiku lotsatira, Msamariya uja anapereka ndalamu kwa mwini nyumba ya Alendo namulangiza kuti amusamalire munthu wopwetekedwayo. “Msungire iye, ndipo chiru chonse umpsata koposa, ine, pobwera, ndidzakubwezera iwe.”

Yesu ananena fanizoli pofuna kuyankha funso limene katswiri wina wa malamulo anafunsa. Yesu ndi katswiri wa malamuloyo anagwirizana pa mfundo yakuti moyo

(Yapitirira pa tsamba 2)

Mau a Mkonzi

Tsamba 3

Kusanthula Mau a
Mulungu: Ntchito za
Chifundo

Tsamba 4

Nkhani yothandiza pa
kusanthula Baibulo:
Ntchito za Chifundo

Tsamba 5-6

Mafunso & Mayankho

Tsamba 7

Kodi Mukudziwa?

Mau a pa Nyengo yake

Tsamba 8

ZIMENE BAIBULO

Limaphunzitsa za...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;

Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyeria

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;

Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;

Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;

1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;

1 Akor. 7:10-11

Chikhaliidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;

Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba I)

wosatha umaperekedwa kwa iwo amene amakonda Mulungu ndi mtima wao wonse komanso kukonda anzawo monga amadzikondera iwo eni. Koma katswiri wa malamuloyu anafunsa kuti, "Ndipo mnansi wanga ndani?" Kenaka Yesu anamuphera fanizo ili la "Msamariya Wachifundo."

Mnzake weniweni sanali munthu wa mtundu wake kapena wa chikhaliidwe chake. Sanali uyo amene anali wokhulupirika popembedza mu kachisi. Mnzake weniweni anali mlendo, iye amene anadzipereka kumuthandiza pa nthawi imene amasowa chithandizo. Uwu ndiye mtundu wa chikondi chimene chimatsekula zipata za kumwamba.

Moyo wosatha, ngakhale uli mphatso ya kwa Mulungu, umaperekedwa kwa iwo amene akonda Mulungu komanso anthu anzawo. Chikondi si mu mau okha komanso mu ntchito. Alipo ambiri mu dziko lathuli, amene ena ali kutsidya la Nyanja, ena ali pafupi pompa kungowoloka mseu, amene akuvutika ndipo afuna thandizo.

Chikhristu chenicheni chimaonetsa chikondi cha Mulungu pamene tithandiza anthu amene paokha sangathe kudzithandiza. Awa ndiye maziko a moyo wa chikhristu. Anthu ena amakhazikika pa chiyero chawo ndi kudzipatula namapeputsa udindo wopereka ndi kuthandiza ku zosowa za anthu za kuthupi, m'maganizo ndi zauzimbu. Msamariya, amene anatumikira ku zosowa za kuthupi za munthu wovulazidwa uja, anali chitsanzo cha Khristu cha munthu amene anakonda mnzake monga iye mwini. Choncho zimene Yesu anauba katswiri wa malamulo uja akunenango lero kuti: "Pita nuchite iwe momwemo."

—mws

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Uthenga Wabwino wa Choondi ndi uthenga wa mkalata umene umasindikizidwa m'dzina la Ambuye kwa anthu onse ku maiko onse ndi cholinga chofuna kuwakhazikitsa ndi kuwalimbikitsa mu choondi cha Mau a Mulungu. Kalata uyu akuphunzitsa ndi kulimbikitsa zonna za Baibulo zimene zakhazikitsidwa kuyambira pa nthawi ya Khristu ndi ya atumwi.

Mau a Mulungu ndi okhawo amene ali muyeso wovomerezeka wa chikhulupiriro. Amaphunzitsa chipulumutso ndi mamasulidwe kuchokera ku uchimo kudzera mu ntchito ya maomboledwe ya mwa Yesu Khristu; komanso kudzazidwa ndi Mzimu Woyeria kumene kumatsatirapo. Ndipo kumatithandiza kuti titsogolere, tiwongolere ndi kuwapatsa ena mphamvu; komanso tikhale ndi chiyero choonekera pa gawo liliolone la moyo wa munthu kuphatikizapo mgwirizano ndi umodzi wa anthu a Mulungu. Utumiki wovomerezeka wa kwa Mulungu uli mu mwa anthu amene ubale wao wachikondi wazikika pa choonadi.

Akonzi: Michael & René Smith

KUTI MULANDIRE NAWO KALATAYI

Uthenga Wabwino wa Choondi ndi uthenga wa kalata umene timasindikiza miyezi itatu illiyonse molingana ndi chitsogozzo cha Ambuye. Kuti mulandire nawo kalatayi mwaulere pa email, pitani pa intaneti ndipo mutipeza pa www.thegospeltruth.us. Muli omasuka kutitumizira maina ndi ma email a anthu amene akufuna kulandira nawo kalatayi. Mainawa muwatumize kwa mikonzi.

KUTI MUTIPEZE

Uthenga Wabwino wa Choondi imasindikizidwa mu maiko osiyanasiyana kuti igawidwe m'maikowo.

Ntchito yosindikiza kalatayi komanso mautumiki ena ochitika ndi ofesi yathu pothandiza kufalitsa uthenga wabwino amathandizidwa ndi zopereka zafulu zoperekedwa mdzina la mpingo wa Mulungu.

Mau a Mkonzi



Indetu ndinena kwa inu, Chifukwa munachitira ichi mmodzi wa abale anga, ngakhale ang'ono ang'ono awa, munandichitira ichi Ine. —Mateyu 25:40

Yesu analakanitsa nkosa ndi mbuzi, opulumutsidwa ndi iwo amene sanapulumutsidwe, potsatira muyeso wa kuchita ntchito zachifundo. Pamenepa sikuti tikunena kuti chipulumutso nchosafunikira, ndipo Khristu anaotsera

kufunikira kwa ntchito zachifundo ndi zaumunthu. Pokhala anthu a Mulungu, kodi anthu ambiri angathe kupeputsa mphamvu ya zachifundo? Kodi mphamvu ya chikhulupiriro kapena chiyero changwiro ngati palibe chikondi chimene chimabweretsa kudzipereka kodzikhuthula kwa iwo amene ali wosautsika ndi wopsinjika?

Pamene tikutumikira ku zosowa za anthu ena, timatumikira Khristu mwini – kupereka kapu ya madzi, kuchereza odwala, kuwayimbira nyimbo iwo amene akhumudwa, kunena mau okoma kwa okalamba, kupereka ma bulangete kwa amene amagona pamphepo, kupereka buledi kwa iwo anjala, kumanga mabala a iwo amene ali ndi zilonda zochucha magazi. Kupereka kwa munthu wosowa ndi chinthu cha mtengo wake komanso chimapereka mwayi ndiponiso mdaliso wodabwitsa. Zinthu zina zimene zimabweretsa chimwemwe pa moyo wanga zachokera ku kupereka kodzikhuthula. Ndazindikiranso kukhala m'moyo opanda kanthu ndipo nkuezeza kuti woyerwa mtima wina wakumana ndi chosowa changa. Nzodabwitsa kwambiri mmene Mulungu anakonzerza dongsolo la chipulumutso.

Ndimakonda choonadi ndi ziphunzitso za Mau a Mulungu. Chokhumba changa ndicho kukweza pamwamba mbendera ya Khristu ndiponiso chiyero chochitachita cha moyo. Mu kalata ya Uthenga Wabwino wa Choonadi ya ulendo uno, ndikulimbikitsa chipunzitso chofunkirachi cha kuchita zachifundo. Pokhala ana a Mulungu, miyoyo yathu idzitsogoleredwa ndi chikondi ndipo idzadze ndi ntchito zachifundo kwa anthu ena. Ichi si chinthu chongopanga mongochitapo basi kapena kuti zindichoke. Ndi lamulo lakumwamba limene liri pa mtima penipeni pa Chikhristu.

Anthu ena amanena kuti kuchita ntchito zothandiza anthu, ntchito zachifundo, sikuti ndi kutumikira Mulungu. Ngakhale kuti utumiki waukulu kwambiri ndiwo kulalikira uthenga wabwino ku dziko lapansi, gawo lina la ntchito ya Mulungu ndilo kutumikira kwa amene ali ndi zosowa zosiyanasiyana zimene anthu amakhala nazo nthawi ndi nthawi. Malemba amanena zambiri za nkhaniyi ndipo pemphero langa ndilo lakuti maso athu atsekuke kwambiri ku maitanidwe a Mulungu ku dera limeneli. Amenewa ndi maitanidwe a TONSEFE.

Nthawi zina timadabwa kuti chimene chimawapangitsa anthu kuti pamene abwera kudzamvera uthenga wabwino kuti alandirenso thandizo la ku umunthu. Kodi kuno abwereranji? Pamapeto pa zonse, ndimalimbikitsidwa chifukwa chakuti Yesu mwiniwake anawauza anthu kuti "Indetu, indetu, ndinena ndi inu, Mundifuna Ine, si chifukwa munaona zizindikilo, koma chifukwa munadya mkate, nimunakhuta." Yesu anadyetsabe khamu la anthu chifukwa cha chifundo. Zili chonchonso ndi ifeyo lero, timagawana ndi anthu ena za chikondi cha Yesu Mwini.

Tiyeni tikhale ndi masomphenya ngati a Msamariya Wachifundo kuti tione zosowa zimene zili m'dziko mwathu, ndipo tisaope kupereka zimene tingathe komanso kupereka modzikhuthula.



Zambiri Zili pa
INTANETI

Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone. makalata akale.



Pemphera la Zachifundo

Ngati ndakaniza aumphawi chifuniro chao, kapena kutopetsa maso a amasiye, kapena kudya nthongo yanga ndekha, osadyako mwana wamasiye; (pakuti kuyambira ubwana wanga analeredwa ndi ine monga ndi atate; ndipo ndinakhala nkhoswe ya wamasiye chibadwire ine.)

Ngati ndinaona wina alinkutayika wopanda chovala, kapena kuti wosowa alibe chofunda; ngati ziuno zake sizinandiyamika, ngati sanafunde ubweya wa nkhosa zanga; ngati ndinasamulira ana amasiye dzanja langa, popeza ndinaona thandizo langa kuchipata; libanhuke phewa langa paphalo, ndi dzanja langa liduke pagwangwa.

Yobu 31:16-22

KUSANTHULA MAU A MULUNGU

MUTU: NTCHITO ZA CHIFUNDO

Kuwerenga Malemba: Mbale kapena mlongo akakhala wausiwa, nichikamsowa chakudy cha tsiku lake, ndipo wina wa inu akanena nao, Mukani ndi mtendere, mukafunde ndi kukhuta; osawapatsa iwo zosowa za pathupi; kupindula kwake nchiyani? Momwemonso chikhulupiriro, chikapanda kukhala nacho ntchito, chikhala chakufa m'kati mwakemo. —Yakobo 2:15-17

Mwachidule: Machitidwe a kukoma mtima ndi chifundo ndiwo maziko pa moyo wachikhristu. Chikondi chenicheni cha umulungu ndiponso kuperembedza kwa chikhulupiriro zimaonetsedwa kudzera mu kudziperekira iwo amene ali osowa komanso ali ndi zochepa.

I. Chikondi chimaonet sedwa kudzera mu Ntchito zochitidwa za Chifundo

- A. Mateyu 22:37-40 Maziko a chikondi.
- B. Luka 10:25-37 Msamariya Wachifundo.
- C. 1 Yohane 3:17-18 Chikondi cha ntchito.

II. Zitsanzo kuchokera mu Chipangano Chatsopano

- A. Machitidwe 10:38 Yesu anachita zabwino.
- B. Mateyu 15:32-39 Khamu la anthu lidyetsedwa.
- C. Aroma 15:26-27 Oyera mtima apereka za kwa osauka.
- D. Machitidwe 9:36 Dorika—wodzaza ndi ntchito zabwino.
- E. Chipangano Chakale: Yobu 31:16-22.

III. Munthu amapulumutsidwa kuti alemekeze Mulungu kudzera mu Ntchito

- A. Mateyu 5:14-16 Ntchito zabwino ndizo kuwala ku dziko lapansi.
- B. Aefeso 2:8-10 Kulengedwa kuti tichite ntchito zabwino.
- C. Tito 2:14 Changu chochita ntchito zabwino.

IV. Ntchito Zabwino kapena Zachifundo zikulamulidwa

- A. Yesaya 58:7 Zachifundo zikulamulidwa.
- B. 1 Timoteo 6:17-18 Mukhale wokonzeka kugawana ndi ena.

C. Tito 2:7 Onetsani dongosolo la ntchito zabwino.

D. Tito 3:8 Pitirizani kuchita ntchito zabwino.

E. Ahebri 10:24 Dzitakaseni kuchita ntchito zabwino.

F. Agalatiya 2:9-10 Kumbukirani osauka.

G. Aefeso 4:28 Perekani kwa iye amene ali osowa.

H. Agalatiya 6:10 Chitani zabwino kwa anthu onse.

V. Ntchito za Chifundo Zimaonetsera

- A. Yakobo 1:27 Chipembedzo choona.
- B. Yakobo 2:14-18 Chikhulupiriro chenicheni.

VI. Madalitso mu Kupereka

- A. Machitidwe 20:35 Kupereka nkodalitsika.
- B. Luka 14:13-14 Mphotho yamuyaya.

VII. Chiweruzo Chomaliza

- A. Chivumbulutso 20:12-13 Molingana ndi ntchito.
- B. Mateyu 25:31-46 Kutengera pa ntchito zochitika za chifundo.

Kumaliza:

Koma iye amene ali nacho chuma cha dziko lapansi, naona mbale wake ali wosowa ndi kutsekereza chifundo chake pommania iye, nanga chikondi cha Mulungu chikhala mwa iye bwanji? Tiana, tisakonde ndi mau, kapena ndi lilime, komatu ndi kuchita ndi m'choonadi..

—1 Yohane 3:17-18

NTCHITO ZA CHIFUNDO

Nkhani yothandiza pa kusanthula Baibulo

MAZIKO A CHIKONDI

Yesu ananena kuti lamulo loposa onse ndilo kukonda Mulungu ndipo lachiwiri lake kukonda anzathu monga ife eni (Mateyu 22:37-40). Chikondi si chinthu chongokhala m'maganizo. Ndi chisankho, chogwirika cha mumtima, udindo, cholinga komanso chimene chimatifulumizitsa kuti tichite zinthu. Chikondi pa Mulungu chimaonetseredwa kudzera mu kumvera Mau ake. Chikondi pa anzathu chimaonetseredwa kudzera mu ntchito za ubwino komanso zachifundo. Popanda chikondi chokhala ngati chimenechi, anthu sangakondweretse Mulungu ndipo ndiponso sangathe kukwanirtsa cholinga cha Mulungu pa moyo wao. Moy wa munthu woyerwa mtima ukhale wodzaza ndi ntchito zachifundo.

MSAMARIYA WACHIFUNDO

Msamariya Wachifundo (Luka 10:25-37) Ndiwo muyeso umene Khristu anatipatsa kuti titsatire pamene tikuthandiza osowa. Ngati m'kristu awona munthu wina ali ndi chosowa koma osamuthandiza ngakhale kukhudzika ndi chifundo, kodi chikondi cha Mulungu chingakhale bwanji mwa iye? "Tiana, tisakonde ndi mau, kapena ndi lilime, komatu ndi kuchita ndi m'choonadi" (1 Yohane 3:17-18). Moy wa m'kristu ukhale wodzaza ndi kupita ku tchalitchi, kupemphera kukhulupirira chiphunzitso choona. Pamwamba pa izi uyenerano kukhala wodzikhuthula ndi kuchitapo kanthu chifukwa cha anthu omwe ali ndi chosowa.

YESU ANAPEREKA CHITSANZO CHA NTCHITO ZABWINO

Pa nthawi yake yochepa ya pansi pano, Yesu anayendayenda nachita zabwino (Machitidwe 10:38). Iye sanangolalikira naphunzitsa za Mulungu, komatu anachirtsia odwala. Anayendera ochimwa. Anadyetsa makamu anjala (Mateyu 15:32-39). Iye anali munthu wachifundo chochuluka ndipo anatumikira ku zosowa zakuthupi za osauka. Dorika yemwe anatchulidwa mu Machitidwe 9:36 kuti anali mzimayi yemwe "anadzala ndi ntchito zabwino ndi zachifundo." Oyera mtima a mu mpingo uyu woyamba anapereka mobwerezabwereza kwa osauka (Aroma 15:26-27) ndipo anatumikira kwa osowa. Anthu odziwa mbiri ya mpingo woyamba amakhulupirira kuti kudziperekwa ku ntchito zachifundo ndicho chimene "chinathandizira kwakukulu" kuti chikhristu chifalikire mwansanga. Zoterezi ndi zimene oyera mtima alero akuyenera kudziwika nazo kumadera kwavo ndi m'dziko lonse. Anthu a Mulungu ayenera kudziwika ndi machitidwe awo a chikondi komanso ntchito zaho zachifundo.

NTCHITO ZABWINO ZIMALEMEKEZA ATATE

"Chomwecho muwalitse inu kuunika kwanu pamaso pa anthu, kuti pakuona ntchito zanu zabwino, alemekaze Atate wanu wa Kumwamba" (Mateyu 5:16). Cholina cha ntchito zachifundo sikuti titchuke kapena kuti anthu atione. Komatu, ntchito zabwino zimawunikira kuwala ndi chikondi cha Mulungu mu dziko lino la mdimali. Kudzera mu ntchito zimenezi, dziko lapansili lingathe kuona Atate ndipo likokedwa ku chipulumutso.

KULENGEDWA KUTI TICHITE NTCHITO ZABWINO

NTchito za chifundo szipulumutsa munthu, Komatu ifeyo ndife "olengedwa mwa Khristu Yesu, kuchita ntchito zabwino, zimene Mulungu anazipangiratu, kuti tikayende m'menemo" (Aefeso 2:8-10). Chifukwa cha ichi, chimodzi mwa zolinga zazikulu za mwana wa Mulungu ndicho kuyenda mu ntchito zabwino. Izi zimapitirira pa



ntchito za munthu za chilungamo ndipo zimakhudza kupereka nthawi ndi chuma chifukwa cha zosowa za iwo amene ali m'mavuto. "Wakubayo asabenso; koma makamaka agwiritsé ntchito, nagwire ntchito yokoma ndi manja ake, kuti akhale nacho chakuchereza wosowa" (Aefeso 4:28).

NTCHITO ZABWINO ZILAMULIDWA

Malemba amatiphunzitsa kuti iwo amene ali olemera (ali nazo zochuluka kuposa zimene zimafunkira) ayenera "kuchuluka m'ntchito zabwino" ndi "kukondwera kugawira ena" (1 Timoteo 6:17-18). Woyerwa mtima amalangizidwa kuonetsa "chitsanzo cha ntchito zabwino" (Tito 2:7) ndi kuti "asamalire akhalebe atsogoleri a ntchito zabwino" (Tito 3:8). Mwana wa Mulungu ayenera "asamalitse" chifukwa zosamalira ndi zochitika za moyo uno zikhoza kuyamba moyo wochitira anthu ena zabwino. Masiku ano anthu ambiri ndi odzikonda ndipo safuna kupeza nthawi kapena ndalamu kuti athandizire osowa. Ili ndi vuto

(Yapitirira pa tsamba 6)

*“Monga tili
nayo nyengo,
tichitire onse
chokoma . . .”*



(Kuchokera pa tsamba 5)

Iauzimu. Nchifukwa chake Paulo akuwalimbikitsa oyera mtima kuti “tiganizirane wina ndi mnzake kuti tifulumizane ku chikondano ndi ntchito zabwino” (Ahebri 10:24).

PEREKANI MOLINGANA NDI KUTHEKERA KWANU

Dzikoli ndi lalikulu kwambiri ndipo zosowa ndi zochuluka. Chifukwa chake nkosatheka kuti munthu mmodzi apereke kwa onse amene akuvutika. Ambuye safuna kuti anthu akhale m'moyo wodzitsutsa chifukwa chakuti lye wawadalitsa ngati munthu kapena wadalitsa dziko lawo ndi chuma chochuluka. Monga mmene Mulungu wadalitsira, mwana wa Mulungu agawire monga angakwanitsire. “Chifukwa chake, monga tili nayo nyengo, tichitire onse chokoma, koma makamaka iwo a pa banja la chikhulupiro” (Agalatiya 6:10).

CHIPEMBEDZO CHANGWIRO

Anthu ena amasianitsa moyo wao wauzimu ndi zosowa za umunthu zimene zawazungulira.

Pa Yakobo 1:27 amanena izi mwachimvekere kuti,
“Mapembedzedwe oyera ndi osadetsa pamsaso pa Mulungu ndi Atate ndiwo: kucheza ndi ana amasiye ndi akazi amasiye m'chisautso chao, ndi kudzisungira mwini wosachitidwa mawanga ndi dziko lapansi.” Mwa tsoka, pali anthu amene

amakhazikika pa gawo limodzi kapena linzake la chipembedzo changwiro. Chipembedzo changwiro ndi kukhala oyera ndi osadzidetsa ku dziko lapansi ndi kukhala moyo wopatulika pamsaso pa Mulungu. Chimenechi ndi chofunikira kwambiri, koma chipembedzo changwiro chimakhudzanso ntchito za chifundo–kuyendera ana amasiye ndi amayi amasiye komanso kuwapatsa zosowa zawo za panthawiyo. “tikumbukire aumphawi” (Agalatiya 2:9-10).

CHIKHULUPIRO RO CHOONA

Chipindulo chake nchiyani, munthu akanena, Ndili nacho chikhulupiro, koma alibe ntchito? Mbale kapena mlongo akakhala wausiwa, nichikamsowa chakudya cha tsiku lake, ndipo wina wa inu akanena nao, Mukani ndi mtendere, mukafunde ndi kukhuta; osawapatsa iwo zosowa za pathupi; kupindula kwake nchiyani? Momwemonso chikhulupiro, chikapanda kukhala nacho ntchito, chikhala chakufa m'kati mwakemo (Yakobo 2:14-18).

Chikhulupiro choona ndiponso chipembedzo changwiro sizingokhudzana ndi kukhala munthu wolungama. Zikhudzana ndi chikondi cha Mulungu chimene chigwira ntchito mu mtima ndipo chipangitsa munthu kuti akonde anthu ena. Chikondi ndi chikhulupiro chimenechi chimaonetseredwa pamene tikutumikira kwa osauka. Pali chimwemwe ndi mdalitso waukulu pamene tikhala m'moyo wosadzikonda. Yesu anati, “Kupatsa kutidalitsa koposa kulandira” (Machitidwe 20:35). Anthu ambiri akusemphana ndi mdalitso weniweni umene umapezeka mu ntchito za chifundo. Mphotho yaho yaikulu idzakhala cholowa chimene adzalandira kwamuyaya (Luka 14:13-14).

TIWERUZIDWA MONGA MWA NTCHITO ZATHU

Pa Mateyu 25:31-46 Yesu anapereka chithunzi choonetsera zachisoni zimene zidzachitike pa tsiku la chiweruzo. anthu anaweruzidwa osati molingana ndi mphatso zawo zauzimu, kapena muyeso wa chikhulupiro wao, kapenanso osati moyo wao wosamala za chipembedzo ngakhale mapemphero awo aatali. Iwo anaweruzidwa molingana ndi ntchito zawo zachifundo. Kodi iwo anadyetsa anjala, anaveka amaliseche, anayendera odwala kapena kuchezera andende?

Ambuye atithandize kuti miyoyo yathu isandulike mwa Khristu ndi kuti tsiku ndi tsiku tigwire ntchito ndi kutumikira ndi mtima wothandiza ku zosowa za anthu ena za ku uzimu komanso kuthupi.

—mws

Mafunso ndi

Mayankho

Kodi anthu amene amapereka miyoyo yawo ku kuthandiza aumphawi adzapita kumwamba?

Ayi si kwenikweni. Kupereka ndi kudzikhuthula chifukwa cha anthu ena ndi zotsatira za chipulumutso; koma pazokha izi siziwapulumutsa. Popeza onse anachimwa ndipo ayenera kuti alape ndi kukhululukidwa kudzera mu mphamvu ya Yesu Khristu.



Kodi ndikuyenera kupereka kwa aliyense wosowa amene ndamuona?

Ayi. Monga mmene timachitira ndi gawo lilitlonse la moyo wathu, tiyenera kutsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu. Ngakhale tikuyenera kuchita ntchito zachifundo, nkofunikira kukhala adindo abwino a zimene Mulungu watipatsa kuti tizisamalire. Titati tipereke kwa aliyense wosowa, sitingakhale ndi zokwanira. Ntchito za chifundo ziyambe ndi anthu a m'banja la chikhulupiriro. Umakhala umboni wosakhala bwino pamene munthu apereka ndalama kwa alendo

ndipo mnzawo amene akhala naye pafupi mu chipembedzo akugona nayo njala.

Kuonjezera pamenepa, m'moyo uno, anthu osiyanasiyana ali ndi maitanidwe osiyanasiyana amene akhoza kuwapangitsa kuti akhazikike pa ntchito zaho za chifundo. Munthu mmodzi akhoza kukhala ndi kufulumizidwa kofuna kutumukira ku zosowa za ana amasiye. Wina akhoza kukhala ndi kufulumizidwa kuti athandize anthu ongoyenda mu nsewu amene alibe pokhala. Winanso akhoza kukhala ndi kufulumizidwa kothandiza anthu anjala m'maiko ena. Zosowa zonsezi ndi zofunika. Ndipo pali zosowa zochuluka kuti aliyense akhoza kuthandiza molingana ndi mmene Mulungu amutsogolerera. Komatu kumbukirani, Mulungu akutitsoglera kuti tichite ntchito zabwino.

Kodi kupereka zachifundo kumalimbiktsa khalidwe laulesi ndi losokonekera mwa othandizidwawo?

Limeneli ndi funso lalikulu ndipo chifukwa cha kuchepa kwa malo sitingathe kuyankha mwatchutchutchu. Malemba amatilamula kupereka zachifundo ndipo sitienera kuzichepetsa zimenezi podzilungamitsa ngati kuti ndi zosafunikira. Sichinthu chabwino kupereka ndalama kwa munthu woledzera kuti akamwere mowa. Koma ngati ana a munthu woledzerayo akugona ndi njala chifukwa cha uchimo wa bambo awo, kukhala kwabwino kuwapatsa chakudya ana osalakwawo. Malemba sakulimbiktsa chikhaldwe chongothandiza pa zilizonse, koma nyengo zimene anthu okonda akhoza kuthandiza anjala, amaliseche ndi osauka.

Ngati munthu ali waulesi ndipo amangokhala panyumba osafuna kugwira ntchito, kumupatsa chakudya



kapena ndalama wotereyo kukhaza kuonjezera ulesi wake. Koma ngati munthu sakukwanitsa kupeza ntchito ngakhale akuyesetsa kufunafuna, amenyeo ngoyenera kuthandizidwa.

Kodi pamene ana athu tikuwadyetsa, timawathandiza kuti adzidalire? Ana amasiye alibe bambo kapena mayi kuti awadyetse, choncho malemba amanena kuti titumikire ku zosowa zaho.

Tanthauzo la chipunzitso cha Khristu linali lakuti tithandize anthu amene ali osowadi, osati iwo amene "ayenera" kapena angathe kubweza. "Ndinali m'nyumba yandende, ndipo munadza kwa Ine." Yesu sananene kuti kucherezako kunali kwa anthu amene anamangidwa ngakhale anali osalakwa.

Kodi anthu osauka aletsedwe kupereka zachifundo?

Ayi. Ngakhale kuti anthu olemera ali ndi kuthekera kopereka, Baibulo limatiphunzitsa tonsefe kuti tipereke ndi kudzipereka modzikhuthula ku zosowa za ena. Kupereka si ndalama zokha komanso nthawi yanu. Ngati munthu wosauka sangathe kudyetsa anjala, iye ayenera kuthandiza winanso wosauka pomulimira munda wake, kumumangira nyumba kapena kugawana naye chofunda. Nthawi zonse pamakhala wina wake amene ali ndi chosowa kuposa ifeyo.

—mws




KODI MUKUDZIWA?

Zimene anthu atatu odziwika bwino a mu mpingo woyamba analemba zokhudzana ndi ntchito za chifundo:

Ngati pakati pavo pali wina amene ali wosauka kapena wosowa, ndipo iwo alibe chakudya chilichonse, iwo (omuyandikira) asale kwa masiku awiri kapena atatu kuti apeze chakudya chopereka kwa iwo osowa. — Aristides, 125 AD

Tikudziwa kuti pali ambiri pakati pathu amene adzigulitsa ku ukapolo, kuti awombole anzawo. Ambirinso ena, adipereka ku ukapolo, kuti ndi malipro amene iwo alandire, akhoze kupezera chakudya anzawo. — Clement wa ku Rome, 96 AD

Patsiku limene inuyo musala kudya, musalawe kena kalikonse kupatulapo buledi ndi madzi. Ndipo pa zakudya zimene mumayenera kudya, muwerengere mtengo wake wa zakudya zimene mwasala patsikulo, ndipo perekani ndalamu yake kwa mwana wamasiye, mai wamasiye kapena wina amene akusowa. — Hermas wa ku Rome, (c. 90-140)



Ponya zakudya zako Pamadzi

Ponya zakudya zako pamadzi; udzazipeza popita masiku ambiri. —Mlaliki 11:1

Solomo analimbikitsa owerenga ake kuti “Ponya zakudya zako pamadzi.” Kunena zonna, malemba awa amagwirtsidwa ntchito pofuna kulimbikitsa anthu kuti afese uthenga wabwino pena paliponse. Pamene izi zili zonna, Solomo amakamba makamaka za ntchito za chifundo. Kufesa mbeu za chifundo ndi ubwino kwa anthu onse amene akuzungulirani. Perekani zakudya kwa anthu asanu ndi awiri kapena asanu ndi atatu (v 2).



Ponyani pamadzi onse. Khalani a chifundo kwa anthu amene sakuyenera nkomwe ngakhale iwo amene sakuoneka kuti sangathe kukubwezerani. Chitani zotheka kusamala mwana wa masiye, mayi amene ali yekha wopanda bambo, bambo amene akudwala, okalamba komanso ngakhale uyo ochimwa. Perekani monga mukuchitira kwa Ambuye ndipo musawumire nkomwe.

Mu nthawi yake yoyikika, Mulungu adzakupatsani zochuluka. Timafesa osati kuti tikondweretse thupi lathu, koma Mulungu amabwezera atumiki ake okhulupirika. Adzakubwezerani.

—mws